


AHEBRI, MUTU WACHIWIRI ²

 Kubwera choyamba, ndi kuwaphunzira Malemba, chotero iye akanakhoza kuwafanizitsa iwo ndipo akanawona ngati izo zinali Choonadi kapena ayi. Iye anazitenga izo, Choonadi, mwa Chipangano Chakale. Tsopano, Paulo anali sikolala wa Chipangano Chakale. Ndi angati akudziwa zimenezo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Iye anaphunzitsidwa pansu pa mmodzi wa masikolala opambana a tsiku lake, Gamalieli, sikolala wodziwika. Ndipo Paulo ankachidziwa Chipangano Chakale. Ndipo ine ndikuganiza kugwedzedwa kwake koyamba, monga ine ndinanena mmawa uja, npamene iye anachitira umboni imfa ya Stefano. Chinachake chiyenera kuti chinamugwira Paulo, chifukwa kudutsa mu zolemba zake zonse anakhala akulozera kwa icho, “Ine sindiri woyenera, chifukwa ine ndinazunza Mpingo mpaka ku imfa. Ndine wotsiriza pakati pawo.”

⁹⁵ O, koma Mulungu anali nalo lingaliro losiyana la izo. Iye anali mmodzi wa amuna amphamvu kwambiri a tsikulo.

Muoneni Paulo Woyera, mtumwi wamkulu
Ndi mwinjiro wake wowala kwambiri ndi
wokongola, (wa ndakatulo anatero)
O, uko ndithu kukakhala kufuula kwina
Pamene ife tonse tidzakakomana Uko.

Tsiku lalikulu ilo pamene ine ndidzamuwona iye akulandira korona wa ofera, mphoto ya ofera!

⁹⁶ Ine ndinaina, ndiri ndi cholemba chaching’ono chakale, kuno osati kale litali, pamene iye ankalemba Makalata awa. Ndiyeno iwo anamudulapo mutu wake. Ndipo anamukankhira iye mu ngalande, kuti apite ndi madzi mu ngalandeyo. Ndipo Myuda wamng’ono uyu apo, iye anati, “Ine ndiri nazo mu thupi langa zipsyera za Yesu Khristu. Ine ndinamenyana ndi zirombo ku Efeso, koma ine ndamenya nkondo yabwino. Ine ndawutsiriza mtundawo. Ine ndachisunga Chikhulupiriro. Ndipo kuyambira pano, kwasungidwira kwa ine korona wa chirungamo, yemwe Ambuye, Woweruza wolungamayo ati adzandipatse ine pa Tsiku limenelo. Ndipo si ine ndekha, koma onse omwe akonda kuwonekera Kwake.” Momwe ine ndimazikondera izo! O, ine ndikufuna kuti ndidzawerengeredwe limodzi ndi amenewo! Ife tinkakonda kuyimba nyimbo:

O, kodi inu mungadzawerengeredwe ngati
imodzi ya mkhola Mwake?
Kodi inu mungadzawerengeredwe ngati
imodzi ya mkhola Mwake
Khalani opanda banga mkati, khalani

mukuyang'anira ndi kuyembekezera
mawonekedwe awo kuti mudzawawone;
Iye akudza kachiwiri.

97 Ine ndikufuna kuti ndidzakhale mmodzi wa iwo. Tsopano wolembayu akupitirira, kuti:

*Chotero ife tiyenera tizipereka . . . tcheru chosamalitsa
kwakukulu kwa zinthu zomwe ife tinazimva, kuwopa
kuti pa nthawi iliyonse ife tingazilole izo kutipulumuka.*

98 Monga ife tinaphunzitsira pa izo, mmawa uja, ndime yachiwiri ikuchita nazo, “Ngati . . .”

Pakuti ngati mawu anayankhulidwa ndi angelo . . .

99 Kodi ife tinapeza kuti angelo anali ndani? Aneneri. “Mulungu ankayankhula mu nthawi zamakedzana . . .” Tsopano, iwe umayenera kuti upange, osati lingaliro lathulathu, koma Baibulo. Tsopano mutu woyamba, wa mutu woyamba, ndime woyamba.

*Mulungu, yemwe mu nthawi zamakedzana . . . mu
machitidwe osiyanasiyana ankayankhula . . . kwa
makolo mwa aneneri,*

100 Tsopano iye akupita cha apa, ndipo akunena kachiwiri.

*Pakuti ngati mawu anayankhulidwa ndi angelo anali
okhazikika, . . .*

Ndipo kodi mngelo amatanthauza chiani? “Mtumiki.” Ngati Mulungu anamudzozza mtumiki . . .” Ndiyeno ngati ife tikhala titadzedwa, ife ndife atumiki a Mulungu. Ife tiri atumiki kwa dziko, kazembe wa Kumwamba, tikudzinenera kuti ndife amwendamnjira ndi alendo. Ife sitiri a mdziko lino. Koma ife tikufunafuna Mzinda ukudzawo, womwe wowumanga ndi wowupanga wake ndi Mulungu. Ife sitimakundika chuma pa dziko lapansi lino, komwe mbala zingasweko, ndi njenjete, dzimbiri, ndi chivundi. Pakuti, chuma chatu chiri Kumwamba, komwe Yesu akukhala ku dzanja lamanja la Ufumu. O, chinthu chaulemerero ndi chopambana chake, kuzidziwa zimenezo.

Ziyembekezo zathu
Sizinamangidwe pa china choperewera;
Kuposa magazi a Yesu ndi chilungamo
Pamene pozungulira ponse moyo wanga
uchoka,

Ndiye Iye ali chiyembekezo changa ndi
chikhazikitso.

Pa Khristu, Thanthwe lolimba, ine ndaima;
Maziko ena onse ndi mchenga wotitimira,
Maziko ena onse ndi mchenga wotitimira.

101 Momwe Eddie Pruitt analemba nyimbo imeneyo, mu nthawi ya kuzunzika!

Tsopano, *ngati mawu* anayankhulidwa *ndi angelo anali okhazikika*,... (Pamene atumiki a Mulungu anayankhula Mawu awo, Iwo anaima)... ndipo mphoto iliyonse *inalandira kubwezera kolungama*;

Kodi ife tidzathawa bwanji tsopano, *ngati ife sitikumumva Khristu*, Yemwe akuyankhula kuchokera Kumwamba?

Tsopano penyani.

Ife tidzathawa bwanji, ngati ife tinyalanyaza chipulumutso chachikulu choterechi;... (Taganizani za izo)... *chomwe poyamba chinayamba kuyankhulidwa ndi Ambuye*,...

¹⁰² Khristu anayamba ntchito Yake. Kodi Iye anachita chiani? Ife tikumuwona Iye, momwe Iye... wodzichepetsa, wotsika, momwe Iye sanali munthu wamkulu wodziwika ngati wafioroje. Koma Iye anali wodzichepetsa, wofatsa, waulemu. Iye sanali mlaliki wamphamvu. Liwu Lake silinali kumveka mu msewu.

Koma Yohane ankapita apo monga mkango wobangula. Iye anali mlaliki.

¹⁰³ Yesu anabwera apo, osati ngati mkango wobangula, koma Mulungu akugwira naye ntchito, kumawatsimikizira Mawu. Mulungu anali ndi Khristu. Petro anatero, pa Tsiku la Pentekoste, “Amuna inu aku Israeli, ndi inu omwe mukukhala mu Yudea... Yesu waku Nazareti, Mwamuna wotsimikiziridwa ndi Mulungu pakati panu, mwa zizindikiro ndi zodabwitsa ndi zozizwitsa, zomwe Mulungu ankazichita mwa Iye, pakati pa inu nonse, chomwe inu nonse muli mboni.” Penyani momwe iye anasindikizira izo pa iwo. “Inu mukanati mumudziwe Iye.”

¹⁰⁴ Yesu anati, “Inu achinyengo.” Anati, “Inu mumapita kunja ndi kukayang’ana pa dzuwa, ndipo inu... Ilo likafiira ndi motsika, ndipo inu mumati, ‘Kukhala nyengo yoipa.’ Ndipo ngati kuli kowala ndi kwadzuwa, kapena zina zotero, inu mumati, ‘Kukhala nyengo yabwino.’” Anati, “Inu mumakhoza kuzindikira mlengalenga, koma zizindikiro za nthawi, inu simungakhoze kuzizindikira. Pakuti ngati inu mukanandizindikira Ine, inu mukanalidziwa tsiku Langa.”

¹⁰⁵ O, zomwe Iye akanafuula usikuuno. Momwe Mzimu Wake ukufuulira kudzera mwa alaliki Ake, “Ora liri pafupi!”

Ife timazindikira. Ife timawona mabomba a atomiki. Ife timadziwa yemwe ati atenge malo a Clark Gable, ndi yemwe ati achite *izi*, *izo*, kapena *zinazo*; kapena yemwe ati adzakhale purezidenti wachiwiri. Ife timakondweretsedwa mu zimenezo, koma ife sitingakhoze kuzindikira zizindikiro za nthawi. Ife tiri pa mapeto.

¹⁰⁶ Ndi chiani icho? Ife tiri okondweretsedwa kwambiri ndi, “Kodi chaputala chotsatira cha televizioni chikhala chiani?”

“Kodi Susie achita chiani?” kapena kodi dzina la mkazi uja ndi ndani. “Ndipo kodi Arthur Godfrey apita kuti? Kodi iye anena nthabwala yotani nthawi inayo?” Ife, ngati Akhristu, timamata malingaliro athu modzaza ndi zovunda zoterozo, pamene ife timayenera kukhala tiri mu pemphero kwinakwake, ndi kumawerenga Baibulo, kuti tizidziwa zizindikiro za nthawi yomwe ife tiri kukhalamo.

¹⁰⁷ Chomwe chikuchita izo, pa nthawi yathuyi, ndi maguwa ofooka, ndiko kulondola, omwe samafika pansu ndi kubweretsa Choonadi cha Uthenga. Ife tidzasowa kuti tidzayankhire kwa zimenezo mu masiku akudzawa. Ife tisamati tizinyalanyaza chirichonse. Ndipo anthu, pamene ife tiri pano pa Branham Tabernacle uyu, nkumawona zizindikiro ndi zodabwitsa, ndi mphanvu ya Khristu woukitsidwa; ndiyeno nkumadziwa kuti ife tikanaika n—nthawi zathu pa zinthu zina, ndi kumanyalanyaza kuti timve Liwu la Ambuye Yesu, “Ife tidzathawa bwanji, ngati ife tinalanyaza chipulumutso chachikulu choterocho?”

¹⁰⁸ Ndime ya 3, kapena ndime ya 4. Apa ndi pamene ife tinatsirizira, pa ndime ya 4, mmawa uja.

Mulungu nayenso powachitira iwo umboni, . . . (O, mai!)

Mulungu . . . powachitira iwo umboni, . . .

Mvetserani kwa Mawu.

. . . limodzi ndi zizindikiro . . . zodabwitsa, ndi zozizwitsa zosiyanasiyana, . . .

Kodi zozizwitsa zosiyanasiyana ndi chiani? Zosiyanasiyana ndi chiani? Zosiyanasiyana amatanthauza “zambiri.” “Ndi zozizwitsa zambiri, Mulungu ankawachitira umboni.” O Mulungu! Ine ndikudalira kuti Izo zilowerera mu mitima yanu. Mvetserani.

¹⁰⁹ Ndine mmodzi wa azibusa anu, limodzi ndi M’bale Neville pano. Ine ndikufuna kuti inu muzitengere Izo pa zozisunga. Baibulo linati, “Ngati pawuka wina pakati panu, ndipo iye mnena *zakuti-n-zakuti*, ndipo izo nkusabwera pochitika, musati muzimvere izo, pakuti ine sindinayankhule. Koma ngati iye ayankhula mu Dzina Langa, ndipo zomwe anena nkufika pochitika, ndiye muzizimva Izo.” Amen. “Pakuti ine ndiri ndi mneneri ameneyo, kapena mlaliki, chirichonse chomwe icho chingakhale chiri. Ngati chimene iye anena chifika pochitika, ndiye muzimumvera iye.”

¹¹⁰ Tsopano, abwenzi, tiyeni ife tizimumva Iye, Mzimu Woyera akuyankhula pakati pathu, akusonyeza zozizwitsa zosiyanasiyana, ndi zizindikiro, ndi zodabwitsa. Tiyeni tisamangozidutsa Izo pamwamba ngati kuti zochitika wamba. Tiyeni tizikumbukira kuti Izo ndi Yesu Khristu, yemweyo

dzulo, lero, ndi kwanthawizonse; akutsimikizira Mawu Ake. Ife tiyenera kuti tizichita izo. O, chonde zichitani izo. Zisamalitsani. Muzilola chinthu china chirichonse chizikhala chachiwiri, ngakhale kunyumba kwanu, amuna anu, akazi anu, ana anu. Chirichonse chomwe chingakhale chiri, zichiikani icho pachiwiri. Zimuyikani Mulungu poyamba. Inu mukuti, “M’bale Branham, pamwamba pa ana anga?” Pamwamba pa chirichonse. Zimuyikani Mulungu poyamba. Muloleni Iye azikhala woyamba.

¹¹¹ Eliya anabwera kuchokera ku phiri, tsiku lina. Iye anali mngelo, mtumiki, mtumiki wa Mulungu, wodzozedwa. Ndipo iye anamupeza mkazi wamasiye akutola nkhu ni ziwiri. Iye anati, “Pita, kandiphikire ine chitumbuwa chaching’ono, ndi kunditengera ine madzi pang’ono.”

¹¹² Ndipo iye anati, “Momwe inu muliri amoyo, ine ndangotsala ndi zitumbuwa zokwanira zokha, kapena ufa wokanyidwa wokwanira, kuti ndipangire chitumbuwa chofewa chimodzi chaching’ono. Ndipo ine ndatsala ndi mafuta ongokwanira kuti athere limodzi, oti ndisakanizire izo, mwa kufupikitsa. Ndipo ine ndikutola nkhu ni ziwiri.” Kachitidwe kachikale komwe kanali, kachitidwe Kachimwenye, kopingasitsa nkhu ni ndi kuziwotcha izo kuchokera pakati, ndi kumazisonkhezera izo mkati. Ndapangapo moto wambiri wa mu msasa monga choncho. Anati, “Ine ndikuti ndikaphike kamkate kakang’ono ako ka ine ndi mnyamata wanga, mwana wanga. Ndipo ife tikuti tidye izo ndi kufa.” Uko kunali kuli chilala kwa zaka zitatu ndi miyezi isanu ndi umodzi, kunalibe madzi kulikonseko.

¹¹³ Mneneri wolimba uja, wokalamba, anamuyang’ana mkazi uja mu nkhope. Iye anati, “Pitani, kandiphikire ine mkate choyamba.” Kulamula kwakeko, kuti mwamuna amuize mkazi wamasiye, yemwe akufa ndi njala, kuti ayambe wamudyetsa kaye iye. Kodi iye ananena chiani? “Pakuti ATERO AMBUYE, mbiya siuma konse, ngakhale supa siuma, mpaka Mulungu atadzatumiza mvula pa dziko lapansi.”

Choyamba, Mulungu. Iye anapita ndipo anakaphika mkate wawung’ono uwo, ndipo anabwera ndipo anadzawupereka iwo kwa mneneri. Anabwerera mmbuyonso ndi kukaphika wina, ndi wina, ndi wina, ndi winanso. Ndipo mtsukowo sunathe konse, kapenanso supa sinaume, mpaka Mulungu atatumiza mvula pa dziko lapansi. Iye anaika Mulungu patsogolo pa ana ake. Iye anaika Mulungu patsogolo pa china chirichonse. Iye anatenga Ufumu wa Mulungu, poyamba.

¹¹⁴ Mulungu ayenera kuti azikhala ndi malo oyambirira mu mtima mwanu, malo oyamba mu moyo wanu, malo oyamba mu chirichonse chimene inu muchichita kapena chimene inu muli. Mulungu ayenera kuti azikhala woyamba. Iye samafuna malo achiwiri. Iye samayenera kulandira malo achiwiri. Iye

amayenera kulandira zopambana, ndipo zoyamba, ndi zonse zomwe ife tiri nazo. Iye amayenera kulandira zimenezo. Lidalitsike Dzina Lake loyera!

Pakuti Mulungu nayenso pochitira... umboni, iye anaperekera umboni, limodzi ndi zizindikiro ndi zodabwitsa, ... zozizwitsa zosiyanasiyana, ndi mphatso za Mzimu Woyera, molingana ndi kufuna kwake komwe?

¹¹⁵ Osati zimene anthu anena, zomwe mpingo unena, koma chomwe chifuniro cha Mulungu chinali. O, ife tikusowa kuti tizifunafuna chifuniro cha Mulungu, osati kukonedwa ndi oyandikana nawo anu, osati kukonedwa ndi ana anu, osati kukonedwa ndi amuna anu kapena akazi anu. Koma, zifunafunani chifuniro cha Mulungu, ndipo zichitani izo poyamba. Kenako zina zirizonse, chifuniro cha akazanu ndi chifuniro cha ana anu, zizitsatira limodzi ndi icho. Koma, zimuyikani Mulungu poyamba.

¹¹⁶ Penyani, tsopano

Pakuti kwa angelo iye sanaikire kugonjera kwa dziko likudzalo, lomwe ife tikulikambali.

¹¹⁷ Mwinamwake, Angelo aakulu omwe amatumikira Mmiyamba, Gabrieli, Mikaeli, Wuduwomu, ndi makumi a zikwi kuchulukitsa makumi a zikwi za Angelo a Kumwamba; kapena makumi a mazana a aneneri omwe anakhala ali pa dziko lapansi, aliyense wa iwo; Iye sanamuike aliyense wa iwo kuti azikhala ndi ulamuliro pa dziko liri nkudza, lomwe ife tikulikambali. Osati mmodzi! Iye sananene konse, “Yesaya, iwe udzalamulira dziko.” Iye sanaliyike konse dziko kwa kumumvera Eliya. Ngakhalenso Iye sanaliyike ilo kwa Gabrieli, kapena mngelo aliyense, mzimu wotumikira uliwonse.

¹¹⁸ Penyani zomwe iye ananena, Paulo, apabe akumukuza Khristu, zomwe ife tikuzikamba.

Koma wina pa malo ena anachitira umboni, kuti, Kodi munthu ndi chiani, kuti inu mumamulingalira iye? kapena mwana wa munthu, kuti inu muzimuchezera iye?

Inu mwamupanga iye wotsikirapo pang’ono kuposa angelo; inu mwamuveka iye nduwira ya ulemerero ndi ulemu, ndipo munamuika iye kuyang’anira pa ntchito za dzanja lanu:

¹¹⁹ Tsopano, ngati inu mukufuna kuti muwerenge izo, ndi Masalmo 8:4-6, Davide akuyankhula. Tsopano kodi iye anamutcha Davide chiani apa? Izo zikukhazikitsa icho, apo pomwe, ngati zinali zolondola mmawa uja, pa mneneri.

¹²⁰ Iye anati, “Pakuti mmodzi wa angelo ananena pa malo ena.” Davide, mtumiki wa Mulungu, anali mngelo wa Mulungu, pakuti

iye anali mtumiki wa Mulungu. Mngelo anati, Davide anati, mu Masalmo, “Inu munamupanga Iye wotsikirapo pang’ono kuposa Angelo Akumwamba.” Mngelo ananena kuti Mulungu anamupanga Iye motsikirapo kuposa Mngelo, kuti Iye akhoze kumuveka Iye nduwira; ndipo Iye akhoze kumva kuwawa ndi kukalawa imfa, kuti akwezedwe mmwamba kachiwiri. Kuti Iye akhoze kumupanga Iye. . . wolandira zinthu zonse za mdziko. [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.]

¹²¹ Tsopano, m—mu Mateyu 28:18, ife timawerenga izi. Iye atapachikidwa kale ndipo atawuka kachiwiri pa tsiku lachitatu, iye anakomana ndi ophunzira Ake ndipo anawatuma iwo kuti apite mu dziko lonse, kuti akalalikire Uthenga kwa cholengedwa chirichonse. Iye anati, “Mphamvu zonse Kumwamba ndi padziko lapansi zapatsidwa mmanja Anga. Mphamvu zonse Kumwamba, mphamvu zonse padziko lapansi, zapatsidwa kwa Ine.” Chinali chiani icho? Munthu ndi Mulungu anali atalumikizana. Logos inali itapangidwa thupi ndipo inali itaphedwa, ndipo inawuka kachiwiri kwa kulungamitsidwa kwathu, ndipo anali ndiye Emmanuele wodzozedwa kwanthawi za nthawi. Mulungu anasintha malo Ake okhalamo, kuchokera ku Mpandowachifumu mu milengalenga kutali, kubwera mu mtima wa Mwana Wake, Khristu Yesu, kuti azidzakhala moyo ndi kulamulira kwanthawizonse. “Mulungu anali mwa Khristu.” Iye ndi malo otsiriza opumulira a Mzimu.

¹²² Mzimu unkakhala mu kachisi, tsiku lina, inu mukuzidziwa zimenezo, pansu pa hema. “Ndipo Solomoni anamumangira Iye nyumba. Koma, ngakhale ziri choncho, wa Mmwambamwambayo samakhala mu nyumba zopangidwa ndi manja.” “Koma thupi Inu mwandipangira Ine.”

¹²³ Uko mu Bukhu la Machitidwe, mutu wa 7, pamene iye anali kuyankhula, iye anati, “Onse awo anaziwoneratu Izo. Iwo anamumangira Iye hema, Mose anatero, anali ndi hema, ndipo anaika likasa mkati mmenemo, pakuti Mulungu anali pa Mpando Wachifundo. Iye sankakhala mmenemo.” Chabwino.

¹²⁴ Ndiye, “Thupi inu mwandipangira Ine,” thupi la Ambuye Yesu Khristu, lopangidwa motsikirapo kuposa Angelo kuti adzalawe imfa; ndipo si wina koma Wammwambamwamba mwa mmwambamwamba, Khristu; Kalonga wa Mtendere, Mfumu ya mafumu, Ambuye wa ambuye, Mlengi, nyenyezi iliyonse mu mlengalenga.

¹²⁵ O Mulungu! Iye anakhala wotsikirapo kuposa chirengedwe Chake, kuti Iye akhoze kumuwombola munthu (munthu wopanda pokhala, wopanda chithandizo), ndipo anawapatsa iwo pokhala Kumwamba. Iye anasiya maulemerero a Kumwamba. Iye analisiya Dzina lapamwambamwamba lomwe likanakoza kuchulidwa. Ndipo pamene Iye anali padziko lapansi, munthu anamupatsa Iye dzina lotsikitsitsa

lomwe iwo akanakhoza kumupatsa Iye, anati, “Iye anali mwana wapathengo, pakuyamba pomwe.” Anabadwira mu khola, anakulungidwa mu ziguduli za pa msana pa goli la ng’ombe. Analibe malo oti nkupitako, analibe khomo loti nkupitako. Ndipo anali kutchedwa, “Bezezebule,” mfumu ya adierekezi. Iye anachitiridwa molakwika. Iye analavuliridwapo. Iye anatonzedwa. Iye anakanidwa, ndipo anapita ku malo otsikitsitsa, ndipo anadzichepetseraa kwa “Wazachiwerewere woipitsitsa.” Ndi chimene munthu anachita kwa Iye.

¹²⁶ Koma Mulungu anamukweza Iye mmwamba mokwera kwambiri mwakuti Iye amachita kuyang’ana pansi kuti akuwone Kumwamba. Munthu anamupatsa Iye mpando wotsikitsitsa, anamupatsa Iye malo oyipitsitsa, dzina lotsikitsitsa. Mulungu anamukweza Iye mmwamba ndipo anamupatsa Iye Mpando wapamwambamwamba, ndi Dzina lapamwambamwamba. Ndiko kusiyana kwake chimene munthu anachita kwa Mwana wa Mulungu, ndi chimene Mulungu anachita kwa Mwana wa Mulungu.

¹²⁷ Iye anadzichepetsa, kuti ife tikhoze kukwezedwa. Iye anakhala ife, kuti ife kupyolera mu chisomo Chake tikhoze kukhala Iye. Iye anabwera kwa opanda kwawo, ndipo anadzakhala wopanda kwawo Iyemwini, kuti ife tikhoze kukhala ndi kwathu. Iye anabwera kwa odwala ndipo anapangidwa kudwala Iyemwini, kuti ife tikhoze kuchiritsidwa. Iye anabwera kwa wochimwa, “ndipo anapangidwa tchimo, Iyemwini,” kuti ife tikhoze kukhala opulumutsidwa.

¹²⁸ Palibe zodabwitsa kuti Iye anakwezedwa. Palibe zodabwitsa kuti Iye ali yemwe Iye ali usikuuno. Mulungu wamukweza Iye, ndipo mphamvu zonse Kumwamba ndi dziko lapansi zapatsidwa kwa Iye.

¹²⁹ Pamene ntchito Yake ya pansi pano inali itatha, kuno pa dziko lapansi. Iye anabwera ku dziko lapansi, mwamsanga pamene Iye anatero, nyenyezi ya mmawa inamutcha Iye kuti ndi Mwana wa Mulungu. Iye anamgweza mdierekezi aliyense yemwe Iye anakomana naye. Likhale lodala Dzina la Ambuye! Adierekezi ananjenjemera ndipo anagwedezeka, ndipo anapempha chifundo, mu Kukhalapo Kwake. Inde, bwana. Gehena yense ankadziwa yemwe Iye anali.

¹³⁰ Ankayenda modzichepetsa, Iye analibe malo woti nkuikapo mutu Wake, usiku wa mvula. Zinyama zomwe zimene Iye anazilenga, “Mbalame za mlengalenga ziri ndi zisa, ndipo nkhandwe ziri nazo mphanga, koma Mwana wa munthu alibe malo oti nkuikapo mutu Wake wodawo.” Zedi, Iye anali.

¹³¹ Iye anadzakhala tchimo, anadzakhala wotsika ndi wokanidwa. Koma adierekezi ankadziwa yemwe Iye anali. Iwo anapempha chifundo. Iwo anati, “Chifukwa chiani Inu mwabwera kuti mudzatizunze ife nthawi yathu isanafike.”

Ndipo pamene alaliki ankamutcha iye, “Belezebule,” wambwebwe; adierekezi anali kumutcha Iye, “Mwana wa Mulungu wamoyo,” ndi kumapempha chifundo.

¹³² O, momwe ife tingakhoze kungoima kwa miniti yokha! Kodi inu nndani, mulimonse? Kodi ntchito yomwe muli nayo ija imatanthauza chiani? Kapena kodi nyumba yaing’ono yathu ija imatanthauza chiani? Kodi galimoto yomwe ife tiri nayo imatanthauza chiani?

¹³³ Msungwana wamng’ono wokongola, iwe kanthu kakang’ono kosasatizidwa, kodi mawonekedwe aang’ono awo omwe iwe uli nawo tsopano angachite chiyani? Inu anyamata muli ndi tsitsi lonyezimira, loterera, mapewa owongoka; inu mudzapindika pansu tsiku lina, pamene mudzaweramitsidwa ndi usinkhu.

¹³⁴ Koma, adalitsike Ambuye! Inu muli ndi solo yomwe ili yobadwa kachiwiri. Inu mudzakhala moyo kwa nthawi ndi nthawi, chifukwa Iye anakhala inu, kuti inu kupyolera mu chisomo Chake mukhoze kukhala Iye, ndi kukonza malo a inu.

¹³⁵ O, ife omwe tikuganiza kuti tiri nazo zovala zosintha, ndi magolosale pang’ono mnyumba, kodi ife ndi chiani? Mulungu akhoza kuzitenga izo mu mphindi. Mpweya wanu womwe uli mdzanja Lake. Ndipo pano pakati pathu kuti achize odwala, kulengeza ndi kuvomereza, ndi kuneneratu, ndipo nthawi iliyonse mwangwiro. Ndipo ngakhale kukhuzidwa mokwanira kuti abweretse nsomba yaing’ono, yakufa kubwerera ku moyo wake kachiwiri, pakati pa ife. Yehova pozungulira ife, Yehova mkati mwathu, INE NDINE wamkulu ndi wamphamvu.

¹³⁶ Pamene Iye anafa, iwo ankaganiza kuti iwo athana naye Iye. Iye anakwera kupita mu hade. Pamene Iye ankachoka pa dziko lapansi tsiku lijali pamene Iye anapachikidwa, Iye anapita ku madela a otaika. Baibulo linati, “Iye anapita nakalalikirira kwa miyoyo yomwe inali mu ndende, yomwe siinalape mu kuvutika motalika, mmasiku a Nowa.” Pamene Iye anafa, ndipo mzimu Wake utamuchokera Iye, Iye anakhala Logosi kachiwiri. Iye, ine ndikuwona, anati, “Ine ndinabwera kuchokera kwa Mulungu. Ine ndikubwerreranso kwa Mulungu.”

¹³⁷ Ndipo Mulungu anali Lawi la Moto lija lomwe linkawatsogolera ana mu chipululu. Ndipo pamene Iye anali kuno pa dziko lapansi. . . Ndipo pamene Iye anafa, Iye anabwerreranso ku Kuwala kachiwiri. Paulo anamuwona Iye, ndipo Iye anali Kuwala. Palibe wina aliyense wa iwo anamuwona Iye. Iwo anamuwona Paulo akugwa. Chinachake chinamukhudza iye, ndipo Iko kunali Kuwala. Paulo anati, “Nndani Yemwe ine ndikumuzunza?”

¹³⁸ Iye anati, “Sauli, Sauli, chifukwa chiani iwe ukundizunza Ine?”

Anati, “Ndi ndani Uyo?”

139 Iye anati, “Ine ndi Yesu, yemwe iwe ukumuzunza, ndipo ndi kovuta kuti iwe uzimenyana ndi zisonga.”

140 Ndiye iye anapita nakaphunzira za Kuwalako. Paulo anabwerera mu Baibulo, kuti akafufuze kuti Kuwalako kunali chiani. Ndipo iye analemba Kalata iyi. Iye ali Yehova yemweyo. Kuwala komwe kuja komwe kunali mu chipululu ndi ana a Israeli. Ndipo pamene Petro anali mu ndende, Iye anali Kuwala kumene kunabwera ndipo kunadzatsegula zitseko.

141 Ndipo mwa chisomo Chake, chotero wina asadzakhale ndi chowiringula chirichonse...O, ngati iwo akanakhoza kuwaiwala atumiki osaphunzira, ndi kukumbukira: si mtumikiyo, ndi Uthengawo. Iye wabwera pansu kachiwiri, ali ndi ife, mu mawonekedwe a Lawi la Kuwala. Ndipo Iye akuyenda ndi zozizwitsa Zake zomwe zija ndi zizindikiro, palibe chomwe chiri kunja kwa Baibulo; kukhala limodzi ndi Baibulo, kuligwirizira ilo pansu pa kumvera, kutulutsira kunja ulemerero Wake, kusonyeza mphamvu Zake. Lidalitsike Dzina Lake loyera!

142 Ine ndikudziwa inu mukhoza kuganiza kuti ine ndapenga; koma, o, Mpumulo Wamuyaya wodala uwo womwe uli mu solo yanga. Ngakhale mikuntho igwedezze, nangula wanga wagwira mkati mwa chotchinga.

143 Ndipo kumuwona Iye pamene Iye ankafa, mpaka, mwezi unadzigwetsa chafufumimba mwamanjenje. Dzuwa linalowa pakati pa tsiku. Ndipo pamene Iye anapita ku madera a otayika, [M'bale Branham akugogoda kanai paguwa—Mkonzi.] anagogoda pakhomo, ndipo chitseko chinakankhika motsegula. Baibulo limati, “Iye anakalalikira kwa miyoyo yomwe inali mu ndende, yomwe sinalape mu kuvutika motalika mu masiku a Nowa, Iye atamwalira kale pa dziko lapansi lino. M'bale wanga ndi mlongo wanga, pamene Iye anamwalira, ntchito Yake ya pansu pano inatha, koma Iye anali akugwirabe ntchito. Ndipo Iye akadali pa ntchitoyo usikuuno. Amenii.

144 Iye anagogoda pa zitseko za otaika. Baibulo limati Iye anatero. Ndipo Iye anachitira umboni, “Ine ndine Mbewu ya mkazi. Ine ndine Iye yemwe Adamu ankamukamba. Ine ndine Yemwe Enoki anati akanadzabwera ndi zikwi khumi za oyera Ake. Ine ndine Mwana wa Mulungu wamoyo, ndipo inu munachimwa nkuchoka mu tsiku lanu la chisomo. Koma izo zinaloseredwa kwa inu, ndi angelo, Enoki, Nowa, kuti ine ndiyenera kuti ndibwere kuti ndidzakwaniritse Mawu aliwonse a Baibulo la Mulungu. Ine ndiri pano ngati mboni mu 'dziko lino la otaika.” Ndipo Iye analalikira kwa iwo.

Mpaka pansu ku hade Iye anapita, anagogoda pa zitseko mu hade. Mdierekezi anatsegula chitseko, anati, “Ine ndakupeza Iwe tsopano.”

¹⁴⁵ Analanda mafungulo awo kuchokera pa mbali yake, anati, “Iwe Mdierekezi, iwe wagwira chinyengo kwa nthawi yaitali.” Ndi izi apa, apa pomwe mu Baibulo. Ine ndifika kwa izo mu miniti. “Iwe wachita chinyengo kwa nthawi yaitali, koma ine ndabwera kudzakulanda.” Anawatenga mafungulo amenewo ndipo anamukankhiranso iye mkati, ndipo anatseka chitsekocho.

Anabwera modutsa nadzamutenga Abrahamu, Isaki, ndi Yakobo. Pa tsiku lachitatu Iye anauka, ndipo iwo omwe anagona mmanda anauka limodzi Naye. O, aleluya! Palibe zodabwitsa wandakatulo anati:

Pokhala moyo, Iye anandikonda ine; pakufa,
Iye anandipulumutsa ine;
Poikidwa mmanda, Iye anatengera machimo
anga kotalitali;
Powuka, Iye anandilungamitsa mwaulere
kwanthawizonse,
Tsiku lina Iye akubwera, o, Tsiku laulemerero.

¹⁴⁶ Chodala chikhale chimango chomwe chimamanga mitima yathu ndi chiyanjano cha Chikhristu, chikondi cha Mulungu. Pamene Iye anauka, Iye anali asanatsirize, apobe. Iye anali ndi ntchito yina yoti akaichite.

¹⁴⁷ Baibulo linati, “Iye anakwera Mmwamba ndipo anapereka mphatso kwa anthu.” Apo panali chikhalidwe chitalendewera pa dziko lapansi, cha mdima, cha kulunda, cha imfa, ndi kutopa. Mapemphero sakanakhoza kubwera mmwamba, chifukwa Chitetezero chinali chisanapangidwe. Koma, Iye anaswa kupyola mu chotchinga chimenecho. Iye anatsegula njira. Iye anaswa chotchinga cha matenda. Iye anaswa chotchinga cha tchimo. Iye anaswa chotchinga cha kutopetsedwa. Iye anaswa chotchinga cha kufooketsedwa. Iye anaswa chotchinga chirichonse, ndipo anapanga msewuwaukulu wa munthu wolowelera, kumayenda kupita mu msewuwaukulu wa Mfumu. O, mai, pamene Iye anadutsa mwezi ndi nyenyezi, kupitirira pitirira!

¹⁴⁸ Akutsatira, kumbuyo kwa iye, ankabwera oyera a Chipangano Chakale, Abrahamu, Isaki, ndi Yakobo. Iwo anapita mpaka kukalowa mu miyamba ya Kumwamba. Pamene iwo anali kotalitali kuchokera ku Mzinda, ine ndikukhoza kuwawona iwo akukweza maso awo. Abrahamu anati, “Uwo ndi Mzinda umene ine ndinakhala ndikukhumba kuti ndiwuwone. O, tabwera kuno, Isaki. Bwera kuno, Yakobo. O, ife tinali amwendamnjira ndi alendo ku dziko lapansi, koma ndi uwo Mzindawo. Uwo ndi Womwe ife tinkauyembekezerawo.”

¹⁴⁹ Ndipo Baibulo linati iwo anafuula, “Kwezekani mmwamba, inu zipata za nthawi zosatha, ndi kukhala inu mutakwezekana mmwamba, pakuti Mfumu ife Ulemerero ikubwera mmenemo.”

150 Ndipo Angelo kuseri kwa zipata anafuulira mobwezera kwa angelo awa kuseri uku, ndipo anati, “Mfumu ya Ulemerero iyi ndi ndani?”

151 Ndipo angelo kunja uku, aneneri, anati, “Ambuye Wamakamu, Wamphamvu mu Nkhondo.”

152 Ndipo iwo anakanikiza mabatani ndipo chitseko chachikulu chinakankhika motsegula. Kudutsa kumene pakati pa misewu Iye anabwera, Mgonjetsi, motamandika, ali ndi oyera a Chipangano Chakale akuyenda kumbuyo kwa Iye. Anakakhala pansi pa Mpandowachifumu, anati, “Atate, ndi awa apa. Iwo ndi Anu.”

153 Iye anati, “Kwerani pamwamba pano ndi kukhala pansi, mpaka nditawapanga adani Ako onse choponderapo phazi Chako.” Pamene ife tikuwereka, ife tikuzipeza izo apa mu Lemba. Chabwino.

154 Mvetserani tsopano. Ndipo ife tiri pa ndime ya 8.

Ndiye iye waika zinthu zonse mwa kumumvera pansi pa mapazi ake. Pakuti... iye anaika zinthu zonse mwa kumumvera pansi pa mapazi ake, iye sanasiye kanthu komwe sikali... pansi pa iye. Koma tsopano ife sitikuwona... zinthu zonse zitaikidwa pansi pa iye.

Ndiyo, imfa. Ife sitikuiwona imfa, panobe, chifukwa ife tikumafabe. Ife tikuiwona imfa.

Koma, ndime ya 9, “Koma ife tikumuwona Yesu!” Ameni. Mvetserani.

...ife tikumuwona Yesu, yemwe anapangidwa motsikirapo pang’ono kuposa angelo kuti akazunzike mwa imfa, anavekedwa nduwira ya ulemerero ndi ulemu; kuti iye mwa chisomo cha Mulungu akhoze kumulawira imfa munthu aliyense.

Nchifukwa chiani Iye anapangidwa motsika kuposa Angelo? Chotero Iye akanakhoza kulawa imfa. Iye ankayenera kuti afe. Iye ankayenera kuti abwere, kuti adzafe.

155 Yang’ana kuno, mzanga. Usati, usadzaiwale konse izi. Pamene Yesu anali kupita, akuyenda chokwera phiri, imfa inali kulira ikuzungulira mutu Wake.

156 Tiyeni titenge chithunzi chathu mpaka ku Yerusalemu, zaka thuu sauzande zapitazo. Ndipo kodi inu mungakhoze bwanji kuzikana Izo? Ine ndikumva phokoso likubwera kudutsa mu msewu. Chinali chiani icho? Ndi kugunda kwa chinachake. Ndi mtanda wakale wokhukhulizika ukubwera uku, ukutuluka pa zipata za ku Damasiko, ukugunda pa miyala yoyalidwa. Miyala yaikulu yoyalidwa iyo ikadali momwemo. Ukugunda pamwamba pa miyala yaikulu yoyalidwa iyo, gundu-gundu. Ine ndikuwona kukhetsera kwa Magazi pa msewu. Ndi chiani icho? Ndi Munthu yemwe sanachite chopweteka ayi; palibe kupatula

chabwino. Anthuwo anali akhungu. Iwo sanali kumudziwa Iye. Iwo sanamuzindikire Iye.

Inu mukuti, “Wakhungu? Kodi iwo akanakhala ali ndi kupenya kwawo?”

¹⁵⁷ Iwe ukhoza kukhalabe ndi kupenya kwako ndi kukhala wakhungu. Inu mukukhulupirira zimenezo? Baibulo linanena chomwecho. Mukukumbukira Elisha ku Dotani kuja? Iye anapita uko nakawakantha anthuwo khungu, nati, “Tsopano nditsatireni ine.” Iwo anali akhungu kwa iye.

¹⁵⁸ Ndipo anthu ali akhungu usikuuno. Mpingo winawake umene sumakhulupirira mu machiritso Auzimu, anayenda nabwera kwa ine nthawi ina, ndipo anati, “Ndikanthe ine ndi khungu. Ndikanthe ine ndi khungu.” Uko kunali kunyumba ya M^bale Wright. Anati, “Ndikanthe ine ndi khungu.” Anati, “Paulo anamukantha munthu ndi khungu, nthawi ina.” Anati, “Ndikanthe ine ndi khungu.”

¹⁵⁹ Ine ndinati, “Mzanga, Mdierekezi wachita kale izo. Iwe ndi wakhungu kale. Ndithu, iwe uli.”

¹⁶⁰ Iye anati, “Muchize msungwana wamng’ono uyu ndipo ine ndikukhulupirira iwe.”

¹⁶¹ Ine ndinati, “Mpulumutse wochimwa uyo ndipo ine ndikukhulupirira iweyo.” Ndithudi.

¹⁶² “O,” iye anati, “iye ayenera kuti akhulupirira.”

¹⁶³ Ine ndinati, “Chinthu chomwecho apa, izo ziyenera kubwera kudzera mu chisomo chochita mwayekha cha Mulungu.”

¹⁶⁴ Mdierekezi, m—mulungu wa dziko lino, wachititsa khungu maso a anthu. “Iwo ali nawo maso koma iwo sangakhoze kuwona,” Baibulo linatero.

¹⁶⁵ Apa Iye anali, akupita mu msewu, akukhukhuluza mapazi a Magazi mu msewu chokwera. *Njuchi* ya imfa inali ikumuluma momuzungulira Iye, ikulira pa Iye, “Kanthawi pang’ono kokha ndipo ine ndikhala nawe Iwe.” Iye anali kuyamba kufooka, kuchitira ludzu madzi.

¹⁶⁶ Ine ndinawomberedwapo kamodzi, nditagona kuno mmunda, magazi akungochucha kuchokera mwa ine. Ine ndinafuula kufuna madzi. Ndipo bwanawe wanga anathamanga, anakatenga chipewa chake ndipo anachiika icho mmadzi; akale andere, nyongolosi ziri mmadzimo. Anabwera apo, ndipo ine ndinatsegula kamwa yanga; iye anafinya icho. Chifukwa, magazi anali akutuluka ngati kasupe, pamene ine ndinali nditawomberedwa mwa zidutswa ndi mfuti. Ndikumva ludzu!

¹⁶⁷ Ndiye ine ndikudziwa chimene Ambuye wanga ayenera kuti anali, atakhetsa magazi mmawa wonse uja, kuyambira naini koloko mpaka firii koloko madzulo, akutaya Magazi

onse aja. Ine ndikuwona mwinjiro Wake, poyamba, ngati timadontho tating'ono tiri pa iwo. Ndipo madontho onse awo anayamba kukulira ndi kuyendera palimodzi, kupanga kukhavuka kwakukula kwa Magazi, kukumugunda Iye pa mwendo pamene Iye anali kuyenda kumeneko. Amenewo anali Magazi a Emanuele. O, dziko silinali loyenera kwa Iwo.

¹⁶⁸ Koma pamene Iye akupita mmwamba, *njuchi* iyi ikuluma apo pa Iye. Kodi iyo inachita chiani? Iyo potsiriza inamuluma Iye.

Koma, m'bale, aliyense amadziwa, kuti kachiro mbo kapena njuchi, ngati iyo itangokuluma iwe kamodzi, apo iyo imatsirizitsa ntchito yake yoluma. Iyo singakhoze kuluma kenanso. Chifukwa, pamene iyo ichoka, iyo imakoka mbola yake nichoka.

Ndicho chifukwa Mulungu ankayenera kuti apangidwe thupi. Iye anatengera mbola ya imfa mu mnofu Wake, ndipo Iye anasolola mbola kwa imfa. Lidalitsike Dzina la Ambuye! Imfa ikhoza kulira ndi kuluma, koma iyo siingakhoze kukupwetekani inu.

¹⁶⁹ Paulo, pamene iye anamverera njuchi iyo ikulira momuzungulira iye, imfa inali ikubwera apo. Iye anati, "O imfa, kodi mbola yako ili kuti?" Iye akanakhoza kuloza ku Kalvare komwe iyo inasiyidwa mu mnofu wa Emanuele. "Chiri kuti chigonjetso chako? Koma zikomo kwa Mulungu yemwe amatipatsa ife chigonjetso kupyolera mwa Ambuye wathu Yesu Khristu." Inde.

¹⁷⁰ Ife sitikuwona zinthu zonse.

Koma tikumuwona Yesu, yemwe anapangidwa motsikirapo pang'ono kuposa angelo kuti... avutike ndi imfa...

Pakuti zinayenera kwa iye, kwa yemwe kuli— zinthu zonse, kuti mwa iye ife tiri nazo zinthu zonse, pa chiyambi... ana ambiri... ndi kupangidwa woyang'anira wamkulu wa chipulumutso chathu... kupyolera mu kuvutika.

Njira yokha yomwe Iye akanakhalira Woyang'anira wa chipulumutso chathu, Iye ankayenera kuti avutike.

¹⁷¹ Mvetserani ku Mawu okongola awa apa tsopano. Tsopano mvetserani.

Pakuti limodzi iye amene ayeretsa ndi iwo omwe ayeretsedwa ali onse... amodzi:...

O, kodi inu simukuwona Mpesa ndi Nthambi pamenepo? [Osonkhana ati, "Ameni."—Mkonzi.] Onse amodzi.

... pa chifukwa chake iye sachita manyazi kitchedwa m'bale,

Mukuona? Bwanji? Mvetserani, ndime yotsatirayi.

Kunena, ine ndidzalalikira dzina lanu kwa abale anga, pakati pa Mpingo ine ndidzaimba matamando kwa inu.

Ndipo kachiwiri, ine ndidzaika chidaliro changa mwa iye. Ndipo kachiwiri, Taonani ine ndi ana omwe inu mwandipatsa ine.

Pakuti momwe ziriri ndiye pamene ana ali otengera za mwazi ndi nyama, iye aponso mwiniwake momwe momwemo anatenga gawo la zomwezo; kuti kupyolera mu imfa iye akhoze kumuwononga iye yemwe ali nayo mphamvu ya imfa, ameneyo, ndiye mdierekezi;

Ndi kuwaombola iwo omwe kupyolera... kwa... kudzera... chifukwa cha imfa nthawizonse amasungidwa oyenera mu ukapolo umenewu.

¹⁷² Munthu nthawizonse amawopa imfa. Khristu anakhala tchimo, anapangidwa motsika, kuti atengere imfa pa Iyemwini. Ndipo Iye samachita manyazi kukhala akutchedwa “M’bale” wathu, pakuti Iye anayesedwa chimodzimidzi monga ife timayesedwa. Ndipo Iye akhoza kupanga... kukhala wokhalira pakati woyenera, chifukwa Iye anaima nalo yesero la mtundu womwewo lomwe inu mukuima nalo. Ndipo Iye anatenga malo anu, podziwa kuti inu simukanakhoza kuwatenga iwo mwa nokha.

¹⁷³ Chotero, kodi inu simukuwona, m’bale, mlongo? Chinthu chonsechi ndi chisomo. Chonse cha icho ndi chisomo. Si zomwe inu muchita, mulimonse. Ndi zomwe Iye anakuchitirani inu kale. Tsopano, inu simungakhoze kuchita kanthu kamodzi kuti kakuyenerezeni inu chipulumutso chanu. Chipulumutso chanu ndi mphatso. Khristu anakhala tchimo, kuti inu mukhoze kukhala chirungamo. Ndipo Iye ali mtundu woyenera wa Woyang’anira Wamkulu wa chipulumutso chathu, chifukwa Iye anavutika chimodzimidzi monga ife timavutikira. Iye anayesedwapo chimodzimidzi monga ife timayesedwa. Ndipo Iye sachita manyazi kuti azitchedwa “M’bale wathu,” chifukwa Iye amadziwa zomwe ife tikudutsamo nazo. O, lidalitsike Dzina Lake!

Pakuti indedi iye sanadzitengere pa iye mawonekedwe a angelo; koma iye anadzitengera pa iye mbewu ya Abrahamu.

¹⁷⁴ O, mai! Iye sanakhale Mngelo. Iye anakhala Mbewu ya Abrahamu. “Ndipo ife, pokhala okufa mwa Khristu, timatengapo Mbewu ya Abrahamu, ndipo ndife olandira molingana ndi lonjezo.” Mukuona? Iye sanatenge konse mawonekedwe a Mngelo. Iye sanakhale konse Mngelo. Iye anadzakhala Munthu. Iye anakhala Mbewu ya Abrahamu, ndipo anatengera mbola ya imfa mu thupi Lake lomwe, kuti atijanjanitse ife kubwerera kwa Mulungu, ndipo tsopano

wakhala uko ngati Wokhalirapakati. Mai, ife tingakhoze bwanji kukana Izo, mzanga?

175 Mvetserani.

Chotero mu zinthu zonse chinamukakamiza iye kuti apangidwe monga abale ake, kuti iye akhoze kukhala wansembe wamkulu wachifundo ndi wokhulupirika mu zinthu zokhudzana ndi Mulungu, kuti apange chiyanjanitso . . . tchimo la anthu.

176 Kuti Iye akhoze kukhala Woyanjanitsa! Mukuona, panali udani pakati pa Mulungu ndi munthu. Ndipo palibe munthu . . .

Iwo anatomiza angelo, aneneri. Iwo sakanakhoza kutenga malo anu, chifukwa iwo ankayenera kuti azidzipempherera okha. Iwo sakanakhoza kutenga malowo.

177 Ndiye, Iye anatomiza lamulo. Lamulo linali wapolisi yemwe ankatiyika ife mu ndende. Ilo silikanakhoza kutitulutsamo ife. Iye anatumizira lamulo.

Iye anatomiza aneneri, Iye anatomiza olungama, ndi chirichonse, sizikanakhoza kupanga chitetezero. Koma Iye anabwera pansu ndipo anakhala mmodzi wa ife. O, mai!

178 Ine ndikukhumba ife tikanakhala nayo nthawi yochulukira pakali pano, ine ndikanafuna kuti ndikutengereni inu ku lamulo lija la chiwombolo; koma ife tiribe, koma kwa mphindi yokha. Chithunzi chokongola chiri mwa Rute ndi Naomi. Ngati inu mungawone pamenepo, chiyanjanitso, momwe kuti mwamunayo, mwamuna yemwe anali woti awombole otaika ndi malo okugwa, ankayenera kuti akhale wapachibale kwa munthu yemwe anali atawataya malowo. Ndicho chifukwa Boazi ankayenera kukhala ali . . . anali wapachibale kwa Naomi, kuti iye akanakhoza kumutenga Rute. Ndiyeno, iye ankayenera kuti akhale woyenera. Iye ankayenera kukhala ali wokhoza kuti achite izo, kuti awombole zotaika. Ndipo Boazi, pa chipata, anapereka umboni wapoyera, povula nsapato yake, kuti iye anali atamuwombola Naomi ndi zonse zomwe zinali zake. Ndipo iye ankayenera kuti akhale wapachibale.

179 Ndipo ndi chifukwa chomwe Khristu, Mulungu, ankayenera kuti adzakhale wapachibale kwa ife. Ndipo Iye anabwera pansu ndipo anali Munthu. Ndipo Iye anavutika ndi mayesero. Ndipo Iye ankasekedwa, ankaseleulidwa, ndi kuzunzidwa, ndipo sanalabadiridwe, ndipo anatchedwa “Belezebule,” n—ndi kunyozedwa, ndipo namva kuwawa imfa pansu pa chilango chachikulu. Mukuona? Iye ankayenera kuti akhale ali wachibale kwa ife. Iye ankayenera kuti atsutsidwe mwabodza, chifukwa inu mumatsutsidwa mwabodza. Iye ankayenera kuti anyamule matenda, chifukwa inu mumadwala. Iye ankayenera kuti anyamule machimo, chifukwa awo anali machimo anu. Ndipo Iye ankayenera kuti akhale wapachibale. Njira yokha yomwe Iye akanakhoza kutiwombola ife inali yoti akhale wapachibale kwa

ife. Ndipo momwe Iye anakhalira wapachibale kwa ife, ndi pa kutenga mawonekedwe a thupi lochimwa ndi kukhala mmodzi wa ife. Ndipo mmenemo, Iye analipira mtengo natiwombola ife kuti tibwerere mu chiyanjano cha Atate. O, Mpulumutsi wakeyo! Mawu sangakhoze kufotokoza izo.

Pakuti mwakuti iye mwiniwake anamva kuwawa pokhala womvera, . . . ndi wokhoza kuwathandiza iwo amene ayesedwa.

¹⁸⁰ *Kuwathandiza* amatanthauza “kuchitira chifundo.” Apo, chifukwa chomwe Iye anakhalira *ichi*, kuti Iye akhoze kumakuchitirani chifundo inu omwe muli . . . nazo *zakukwera* ndi *zotsika* zanu, ndi *zakulowa* ndi *zakutuluka* zanu zazing’ono, ndi mayesero anu kufika pakukula kwambiri inu nkusakhoza nkomwe kupirira nawo. Iye amadziwa momwe angachitire chifundo nanu. Iye amakhala pamenepo, kuti azitiimira pakati. Iye amakhala pamenepo, kuti azikukondani inu. Ndipo ngakhale inu mungapite motaika, Iye sangakhoze kukusiyani inu. Iye azikutsatiranibe inu ndi kugogoda pa mtima wanu. Palibe wobwerera mmbuyo mnyumba muno koma yemwe Mulungu amagogoda pa mtima wake tsiku ndi tsiku. Ndipo Iye azichita izo utali wonse pamene inu muli achivundi pa dziko lapansi lino, pakuti Iye anakukondani inu. Iye anakuwombolani inu.

¹⁸¹ Andakatulo ayesera, alembi ayesera, anthu ayesera kuti alongosole nkhani iyo ya “chikondi,” ndipo iyo siingakhoze kupezeka mu kulongsola kwa umunthu. Wina anati:

O, chikondi cha Mulungu, kulemera kwake ndi ungwiro!

Kutambalala kwake ndi mphamvu!

Chidzakhhalapo kwanthawizonse chiripo,

Nyimbo ya oyera ndi Angelo.

Ngati ife tikanakhala ndi nyanja yodzaza utoto,

Ndipo mlengalenga mukanakhala polembapo;

Ndi phesi lililonse pa dziko lapansi cholemba,

Munthu aliyense mlembi mwa ntchito;

Kuti alembe chikondi cha Mulungu mmwamba

Zikanakhoza kuwumitsa nyanja gwaa;

Kapena mpukutu sukanakwanira zonsezo,

Ngakhale ukanatambasulidwa kuchokera mu mlengalenga mpaka ku mlengalenga.

¹⁸² Inu simungakhoze kumvetsa konse. Palibe njira yoti ife timvetsere momwe kuti nsembe yaikulu iyo, yomwe Iye anaichita, anabwera pansu ndipo anadzatiyanjanitsa ife kuti tibwerere kwa Mulungu. Ndiyeno Iye anabwerera ndipo anati, “Tsopano, ine sindidzakusiyani inu opanda mtonthozi. Ine

ndidzabwereranso ndipo ndidzakhala ndi inu, ngakhale mwa inu, mpaka kumathero a dziko.”

¹⁸³ Ndipo pano ife tiri lero, tikukhala mu nthawi yotsiriza, ndi Yesu yemweyo, zinthu zomwezo, zizindikiro zomwezo, zodabwitsa zomwezo, chipulumutso chomwecho, Mzimu womwewo ukuchita zinthu zomwezo, Uthenga womwewo, Mawu omwewo, kuwonetsera komweko, mawonetseredwe omwewo, chirichonse. Izo zikutikakamiza ife kuti tisanyalanyaze chipulumutso chachikulu ichi, pakuti ife tidzasowa kuti tidzakayankhire, tsiku lina, pa chimene ife tikuchita naye Mwana wa Mulungu.

¹⁸⁴ Iye ali mmanja mwako usikuuno, wochimwa, wobwerera mmbuyo. Kodi iwe uchita naye chiani Iye? Iwe ukuti, “Chabwino, ine ndizisiya Izo.” Koma, kumbukirani, usati uzichita izo. Palibe njira, konse, ngati iwe uli wochimwa, yoti iwe ungachoke mnyumba muno ndi kukakhala yemweyo. Iwe sungakhoze kuchita izo.

¹⁸⁵ Pilato, usiku wina, anayesera kuti achite izo. Iye anaitanitsa madzi ena ndipo iye anasambitsa manja ake. Anati, “Ine ndiribe kanthu kochita nazo Izo. Ine ndiri chimodzimodzi ngati kuti sindinayambe ndaziwonapo Izo. Ine sindinayambe ndamvapo za Uthenga. Ine sindikufuna kanthu kochita nawo Iwo.” Kodi iye akanakhoza kuwusamba Iwo mmanja mwake? Iye sakanakhoza.

¹⁸⁶ Potsiriza, inu mukudziwa zomwe zinachitika kwa Pilato? Iye anasokonezeka malingaliro ake. Ndipo anapita uko ku Switzerland, komwe ife tinali chaka chatha, tikulalikira Uthenga. Tsopano kuli mbiri yakale yomwe imanena, kuti, kuli dziwe la madzi komwe anthu amabwera kuchokera konsekonse mu dziko, kuti adzaliwone, chaka chirichonse, pa nthawi ya kupachikidwa. Pilato, iye anadziponyeramo yekha kuti afe, podzipha yekha, analumphira mu madzi awa ndipo anadzimiza yekha. Ndipo chaka chirichonse, pa nthawi yomweyo, madzi abuluu amawira kuchokera pa dziwe ilo, kusonyeza kuti Mulungu anawakana madziwo. Madzi sangakhoze konse kutsuka Magazi a Yesu nkuwachotsa mmanja mwako kapena solo yako. Ilipo njira imodzi yokha yochitira izo, ndiyo kuwalandira Iwo ngati chikhululukiro chako chomwe ndi kuyanjanitsidwira kwa Mulungu.

Tiyeni ife tipemphere.

¹⁸⁷ Atate Akumwamba, ife tikukuthokozani Inu usikuuno chifukwa cha Mawu. “Pakuti chikhulupiro chimadza pa kumva, ndi kumva kwa Mawu.” Ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha Yesu. Ndipo pamene ife tikuliwona tsiku lalikulu ili lomwe ife tiri kukhalamo, momwe kuti zizindikiro ndi zodabwitsa, momwe ife tikulolera kuti zinthu izi zitipulumuke. Mulungu, tsegulani maso a anthu mu kachisi muno, usikuuno, kuti iwo akhoze kuwona ndi kumvetsa kuti ife tiri mu

maora otsiriza. Nthawi ikuthamanga. Ife tiribe nthawi yotalika kwambiri yokhalira kuno, ndipo ife tiyenera kuti tizimuwona Yesu. Ndipo ife tidzati tidzawerengedwe ngati achinyengo, pakuti palibe chowiringula mmawa uno. Pamene inu munapereka masomphenya aakulu, amphamvu aja, a bambo aja kubwera kuno, kuchokera komwe mu dzikoli kutali; ndi kumuwona iye, kupyola mthunzi wa chikaiko, akuwuka kuchokera mu chikuku chija, kulandira kupenya kwake. Miyendo yake kukhala yamphamvu, napita kudutsa mu nyumbayi, akusangalala ndi kutamanda Mulungu. Izo zikusonyeza kuti Mulungu akadali wokhozabe mwa miyala iyi kudzutsira ana kwa Abrahamu. Kuwona masomphenya, monga Yesu anati, “Ine sindimachita kanthu mpaka Atate atandisonyeza Ine. Ine sindingathe kuchita kanthu.”

¹⁸⁸ Munthu wakhungu anamutsatira Iye, ndipo anati, “Tichitireni ife chifundo.”

¹⁸⁹ Iye anati, anakhudza maso awo ndipo anati, “Molingana ndi chikhulupiriro chanu, zikhale izo kwa inu.”

¹⁹⁰ Tsopano, Ambuye, ife tikumuwona Yesu. Ife sitikuwona zinthu zonse. Ife tikuwona ife tikuwatengerabe overa athu ku manda, ndi kumayenda pa manda a wina ndi mzache. Koma ife tikumuwona Yesu, yemwe anapanga lonjezo. Ife tikumuwona Iye ali ndi ife. Osati Yesu mmanda, osati Yesu zaka zikwi ziwiri zapitazo; koma Yesu usikuuno, yemwe ali ndi ife. Ife tikumuwona Iye akuwonetseredwa mu mphamvu Yake yonse, ndi zizindikiro, ndi zodabwitsa.

¹⁹¹ Mulungu, ife tisati tichinyalanyaze Chipulumutso chachikulu ichi. Mulole ife tichikumbatire Icho, ndi kuchilandira Icho, ndi kukhala olemekeza, ndi kumakhala moyo mwa Icho mpaka tsiku lomwe Yesu adzadze kudzatitengera ife Kwathu. Perekani izi, Ambuye. Ife tikupempha izi mu Dzina Lake.

¹⁹² Ndipo pamene ife tiri ndi mitu yathu itaweramitsidwa, ine ndikudabwa ngati alipo munthu mnyumba muno usikuuno, pansu pa Kukhalapo Kwaumulungu kwa Mzimu Woyera, angati, “M’bale Branham, ine ndakhutsidwa kuti ine ndimalakwitsa. Ine ndakhutitsidwa kuti ine ndimalakwitsa. Mulungu waululira kwa ine machimo anga. Ndipo ine ndikudziwa kuti ine ndimalakwitsa. Ine ndikwezera dzanja langa kwa Iye ndi kupempha chifundo, usikuuno. Mulungu, ndichitireni ine chifundo. Ine ndimalakwitsa.” Kodi inu mungachite izo?

¹⁹³ Pamene ife tikuyembekezera mphindi yokha, ngati pali munthu pano yemwe akufuna kutero, pali ubatizo womwe uti uchitike mu mphindi yokha. Ndipo ngati inu muli wochimwa, ine ndikanati ndilape. Inu mungachikane bwanji chikondi chosafanizitsidwa choterocho cha Mmodzi yemwe anafa? Mulungu woyera wa Kumwamba anadzakhala Munthu

wauchimo; osati chifukwa choti Iye anachimwa, koma chifukwa Iye anali ndi machimo anu, ndipo anawanyamulira iwo uko ku Kalvare. Ndipo inu simungavomereze kukhululukidwa kumeneko? Kodi inu simuchita izo usikuuno? Pamene ife tiri ndi mitu yathu yoweramitsidwa, winawake akuti, “Ndikumbukireni ine, M’bale Branham. Ine ndikukwezera manja anga kwa Khristu, ndi kuti, ’Khalani achifundo kwa ine. Ine, ine ndimalakwitsa, ndipo ine ndikufuna kuti ndiyanjanitsidwire kwa Mulungu.” Kodi inu mungakweze dzanja lanu?

Chabwino, ngati aliyense ali Mkhristu, ndiye, tiyeni ife tipemphere.

¹⁹⁴ Atate, ife tikukuthokozani Inu usikuuno, kuti aliyense muno ndi Akhristu, kuti iwo achitira umboni chomwecho pokhala chete, kuti machimo awo onse ali pansu pa Magazi. Ndipo ndine wothokoza kwambiri chifukwa cha icho. Adalitseni iwo, Ambuye. O, ndine wokondwa kwambiri kuti iwo apeza chiyanjaniitso kupyolera mu kupereka nsembe ya Magazi, pa kumva Mawu. Kutsuka kwa madzi, mwa Mawu. Iwo amatitsuka ife. Iwo amatibweretsa ife ku malo aakulukulu, k—komwe wochimwa, ndi mdima wake woipa, amapangidwa woyera ngati chipale. Madontho ofiira a tchimo atatsukidwa nachoka, ndipo ife ndife zolengedwa zatsopano mwa Khristu. Momwe ife tikuthokozera izo, Inu, pa izi.

Tsopano utumiki wa ubatizo ukubwerapo. Ine ndamva kuti dona wamng’ono uyu, usikuuno, ali woti abatizidwa komwe kuno, mu Dzina la Ambuye wake.

¹⁹⁵ O Atate Akumwamba, ife tikupemphera kuti Inu mumudalitse mkazi wamng’ono uyu. Momwe malingaliro anga akupita mmbuyo ku masiku pang’ono okha apitawo, ndikubwera uko mu Henryville ndi kumuwona msungwana wokondedwa wamng’ono uyo akuyenda kuzungulira kumeneko pa msewu. Ndipo usikuuno, iye ndi mayi, dona. Iye wakuvomerezani Inu ngati Mpulumutsi wake wake. Moyo wakhala uli wovuta kwa mwanayu, Ambuye, O Mulungu, koma Kumwamba ndi kotsimikizika kwa iye. Ndipo ife tikukuthokozani Inu pa izo. Ife tikupemphera, Mulungu, kuti Inu mumudalitse mkazi wamng’onoyu tsopano. Ndipo pamene iye akubwera kuti adzabatizidwe ndi madzi, mutamudzaza Iye ndi Mzimu Woyera wa Mulungu. Perekani izi, Ambuye. Mulole moyo wake ukangokondowedwa, kupita Mmiyamba! Perekani izi kwa ulemerero Wanu. Ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.

[Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.]

¹⁹⁶ Ine ndikufuna kuti ndiwerenge kuchokera mu Machitidwe, mutu wachiwiri; Petro akuyankhula, pa Tsiku la Pentekoste, ubatizo woyamba umene unayamba wachitikapo mu Mpingo wa Chikhristu. Petro, akuwadzudzula Afarisi ndi anthu akhungu,

chifukwa chosamuzindikira Mwana wa Mulungu; akuyankhula za momwe Mulungu anamuutsira Iye, ndipo anatsimikizira ntchito Zake, mwa zizindikiro zazikulu ndi zodabwitsa. Mvetserani kwa izi, pamene iye anali kuyankhula. Iye anali akumukweza Yesu.

¹⁹⁷ Mzimu wa Mkhristu aliyense umamukweza Yesu, osati kokha ndi milomo yanu, koma ndi moyo wanu. Milomo yanu ikhoza kunena chinthu chimodzi, moyo wanu nkumachita china. Ngati inu muchita zimenezo, inu mukudziwa chomwe izo ziri? Ichu ndi chinyengo. Ndipo ine kulibwino ndidzakomane nako Kumwamba ndiri munthu wachikunja kusiyana ndi wachinyengo. Ine ndingatenge mwayi wanga mwabwinoko, ine ndikukhulupirira, Kumwamba, ng—ngati wachikunja, kusiyana ndi kukhala wachinyengo. Ine ndithudi... Ngati inu mumachitira umboni za Yesu ndi kumati “Iye ndi Mpulumutsi,” inu muzikhala moyo monga choncho, chifukwa anthu aziyembekezera zimenezo kuchokera kwa inu. Ndiko kulondola. Inu muzikhala moyo monga Mkhristu ayenera kumakhalira. Ife tinadutsa mu izo mmawawu.

¹⁹⁸ Tsopano, Ambuye akalola, mawa usiku, kapena... Lachitatu usiku, ife titenga mutu wachitatu uwu, umene uli mutu wopambana. Ndipo tsopano, mutsimikize kuti mudzabwere Lachitatu usiku. Ndi angati akumva kukoma Bukhu ili, la kuphunzitsa kwa Sande sukulu uku? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] O, zikomo inu mochulukwa kwambiri. Ndizo zabwino.

¹⁹⁹ Tsopano, ine ndikufuna kuti ndiwerenge tsopano kuchokera mu Machitidwe, mutu wa 2, kuyambira pa ndime 32.

Yesu uyu Mulungu wamuukitsa, kwa yemwe ife... tiri mboni. (Iwo ankadziwa izo.)

Chotero pokhala ali chaku dzanja lamanja la Mulungu atakwezedwa, ndipo atalandira kuchokera kwa Atate lonjezo la Mzimu Woyera, Iye watsanulira apa ichi, chimene inu tsopano mukuchipenya ndi kuchimva.

²⁰⁰ Tsopano mvetserani kwa iye akuyankhula za Davide, mmodzi wa angelo.

Pakuti Davide sanakwere kupita kumwamba ayi: koma iye ananena iyemwini, AMBUYE anati kwa Mbuye wanga, Khala iwe pa dzanja langa lamanja,

Kufikira Ine ndiwapange adani ako chopondapo mapazi ako.

Davide sakanakhoza kupita kumwamba; iye anali pansu pa magazi okhetsedwa a ng’ombe, ndi mbuzi, ndi nkhusa. Koma tsopano iye akhoza kuuka; iye anali pansu pa Magazi a Ambuye Yesu. Pakuti iwo ankangoyankhira kwa Magazi awo pamene Iwo akanati adzabwere mwa mphamvu. Pamene

Magazi a Khristu abwera mwa mphamvu, onse awo omwe anali atafa mochitiridwa ubwino, anauka, ndiko kulondola, ndipo anakwera kupita ku Ulemerero.

²⁰¹ Tsopano mvetserani.

Chotero lolani nyumba yonse ya Israeli idziwe. . . (Mvetserani kwa izi). . . kuti Mulungu wamupanga Yesu uyu yemwe, amene inu. . . munampachika, kukhala zonse Ambuye ndi Khristu.

Nanga bwanji zimenezo? Kodi Iye ndi Munthu wachitatu wa utatu, kapena kodi Iye ndi utatu wonsewo? Iye ali uthunthu wonse wa Umulungu, muthupi.

²⁰² Palibe chinthu choterocho monga Amulungu atatu: Mulungu Atate, Mulungu Mwana, ndi Mulungu Mzimu Woyera. Izo mulibe ngakhale mu Lemba, palibe paliponse. Palibe paliponse. Palibe paliponse pamene ife tinalamulidwa kuti tizibatiza, “Mu dzina la Atate, ndi mu dzina la Mwana, ndi dzina la Mzimu Woyera,” palibe paliponse mu Malemba. Ako ndi kachikhulupiriro ka Chikatolika, ndipo izo si za mpingo wa Chiprotestanti. Ine ndimufunse aliyense kuti andisonyeze ine Lemba limodzi pamene munthu wina aliyense yemwe anayamba wabatizidwapo mwa njira ina iliyonse kuposa mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu. Mubwere, mudzasonyeze izo kwa ine, ndipo ine ndiika chikwangwani pa nsana wanga, “Wachinyengo, ndi mneneri wabodza, mphunzitsi wabodza,” ndi kumayenda kudutsa mmisewu. Palibe chinthu choterocho. Palibe konse pomwe aliyense anayamba wabatizidwapo mwa njira imeneyo. Ako ndi kachikhulupiriro ka Chikatolika, ndipo osati chiphunzitsi cha Chiprotestanti.

²⁰³ “Mateyu 28:19,” inu mukuti, “Yesu anati, ‘Pitani inu chotero mu dziko lonse, kaphunzitseni mafuko onse, kawabatizeni iwo mu Dzina la Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera.’” Uko ndi kulondola.

Koma osati, “Mu dzina la Atate, dzina la Mwana, dzina la Mzimu Woyera.” *Dzina* la Atate, *Dzina* (osati maina), la Atate. . .

Atate si dzina. Ndi angati akudziwa zimenezo? Ndi atate angati ali muno? Kwezani manja anu. Ndi ana angati ali muno? Akweze manja awo. Ndi anthu angati ali muno? Kwezani manja anu. Chabwino. Tsopano, dzina lanu ndi ndani? Osati atate, mwana, osatinso munthu.

²⁰⁴ Mzimayi ananena kwa ine nthawi ina, yemwe anali wautatu mosamalitsa, iye anati, “M’bale Branham, koma Mzimu Woyera ndi dzina.”

²⁰⁵ Ine ndinati, “Mzimu Woyera si dzina. Mzimu Woyera ndi chimene Iwo uli. Iwo ndi Mzimu Woyera.” Si dzina; ndi chomwe Iwo uli. Ine ndi munthu, koma dzina langa si munthu. Dzina langa ndi William Branham. Chotero, ngati Iye anati, “Pitani

inu chotero, mukaphunzitse mafuko onse, mukawabatize iwo mu Dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera.”

²⁰⁶ Ndiye Petro, masiku khumi kenako, anati, “Lapani!” Tsopano, apa, mvetserani kwa izi.

Ndipo pamene iwo anamva izi, iwo analaswa mu mtima mwawo, ndipo anati kwa Petro ndi . . .atumwi enawo, Amuna inu ndi abale, kodi ife tichite chiani?

Ndiye Petro anati kwa iwo, Lapani, aliyense wa inu, ndi kubatizidwa mu dzina la Ambuye Yesu Khristu kwa chikhululukiro cha machimo anu, ndipo inu mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera.

²⁰⁷ Ndiye kodi Petro anachita zomwe Yesu anamuuzza iye kuti asachite? Iye sanasokonezeke. Ife ndi omwe tasokonezeke.

²⁰⁸ Pa Machitidwe 2:38, Ayuda anabatizidwa mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu, mwa kumizidwa.

Mu Machitidwe, mutu wa 8, ife tikupeza kuti Filipo anapita uko nakalalikira kwa Asamaria, ndipo anawabatiza iwo mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu, Asamaria.

Mu Machitidwe 10:49, Petro anawalamulira Amitundu kuti abatizidwa mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu.

²⁰⁹ Paulo, Machitidwe 10:5, “Iye anadutsa kupyola maiko aku mtunda aku Efeso, iye anawapeza ophunzira.” Iwo anali ophunzira a Mbatizi; anali, aliyense, Abaptisti. Iwo anatembenuka pansu pa mlaliki wa Chibaptisti dzina lake n—ndi, onani, Apollo. Ndipo iye anali mlaliki wa Chibaptisti, “Ndipo anali kutsimikizira mwa Baibulo kuti Yesu anali Khristu.”

Paulo anati, “Kodi inu munalandira Mzimu Woyera kuchokera pamene inu munakhulupirira?”

²¹⁰ Iwo anati, “Ife sitikudziwa ngati pali Mzimu Woyera uliwonse.”

²¹¹ Anati, “Ndiye inu munabatizidwa chotani?”

²¹² Iwo anati, “Ife tinabatizidwa ndi munthu yemweyo amene anamubatiza Yesu, mu dziwe lamadzilo kumeneko. Ndizo zabwino mokwanira.”


²¹³ Paulo anati, “Izo sizigwira ntchito tsopano. Inu muyenera kuti mukabatizidwa, mobwerezanso.” Ndipo Paulo anawalamulira iwo kuti abatizidwa, mobwerezanso, mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu. Anaika manja ake pa iwo, ndipo Mzimu Woyera unadza pa iwo. Kulondola. Inde, bwana.

Kudzakhala kuwala nthawi yamadzulo,
Njira ya Ulemerero mudzaipezadi;
Kudzera mmadzi, ndiko Kuwala lero,
Kumizidwa mu Dzina la Yesu.

Ana ndi akulu, lapani machimo,
 Mzimu Woyera udzalowamodi;
 Kuwala kwamadzulo kwadza,
 Nzoona Mulungu ndi Khristu ndiwo Mmodzi.

²¹⁴ Ndi zomwe Baibulo linanena. Ndiko kulondola. Ndi ora lake. Ndi nthawi yake yomwe ife tiyenera kuti tilape.

²¹⁵ Mundiuze, mufuule pamene inu muti mukonzeke, mu dziwelo. Ndipo ife . . . [M’bale ati, “Ife takonzeka.”—Mkonzi.] Inu mwakonzeka? Chabwino, kuti akoke zotchinga.

²¹⁶ Tsopano, Ambuye akudalitseni inu tsopano, pamene m’bale akutumikira ubatizo. Kodi inu nonse mukutha kuwona kuno? [M’bale Orman Neville abatiza okhulupirira—Mkonzi.] 

BUKHU LA AHEBRI

Mauthenga khumi ndi umodzi awa a M'bale William Marrion Branham, anaperekedwa mu Chingerezi kuyambira Ogasiti 21 kudutsa Seputembala 22, 1957, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., anatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nadindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2009 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org